Ubatizo Umatithandiza Kuti Tikhale pa Ubwenzi ndi Mulungu (Gawo 2)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 18 m'buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* Bukuli likupezekanso pawebusaiti ya jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso chifukwa chake mumazikhulupirira. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa kenako onani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI MUNTHU AMAFUNIKA KUCHITA CHIYANI KUTI AYENERERE KUBATIZIDWA?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi anthu ena anganene zotani?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

N'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Kuti Mkhristu ayenerere kubatizidwa, ayenera kuchita zinthu zomwe Mulungu amasangalala nazo.
(Werengani mutu 18 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 8-13.)

Werengani Yeremiya 20:9; 2 Akorinto 4:13.
Kodi chikhulupiriro chingathandize Mkhristu kuchita chiyani?

Werengani Machitidwe 3:19.
Kodi Mkhristu ayenera kutsatira zinthu ziti asanadzipereke kwa Mulungu?



Tiyerekeze kuti mwapatsa mnzanu galimoto ngati mphatso. Kodi mungakane kumupatsa makiyi kapena mungakakamire kuti galimotoyo muziyendetsa ndinu? Zimenezi n'zofanananso ndi zimene zimachitika tikadzipereka kwa Yehova. Tikadzipereka, timakhala kuti tamupatsa zathu zonse.

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Kuti munthu abatizidwe, ayenera kudzipereka kaye kwa Mulungu.

(Werengani mutu 18 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 14-16.)

Werengani Deuteronomo 6:15; Maliko 8:34.

Kodi kudzipereka kwa Mulungu kumatanthauza chiyani?

Werengani 1 Petulo 4:2.

Kodi kubatizidwa kumakhudza bwanji zimene Mkhristu amakonda komanso zimene amasankha kuti adzachite?

Kodi panopa mwasintha zinthu ziti kuti muzisangalatsa Mulungu? Nanga mungakonde mutasinthanso zinthu ziti?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

NGATI WINA ATANENA KUTI…

N’zosafunika kuti Mkhristu azilalikira. Mulungu amangofuna kuti tikhale anthu abwino basi.

MUNGAYANKHE KUTI…

Mwinadi anthu ambiri angaganize choncho. Koma ine ndimaona kuti ndimafunika ndizilalikira chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Poganizira zimene munthuyo amakhulupirira, kodi mungamuthandize bwanji pogwiritsa ntchito mfundo ya palembali?

_____

NGATI WINA ATANENA KUTI…

Anthu otengeka kwambiri ndi amene angapereke moyo wawo wonse kwa Mulungu.

MUNGAYANKHE KUTI…

Ndi zoona kuti Mulungu safuna kuti tizingotengeka ndi zilizonse. Koma ndimaona kuti Mulungu *amafuna* kuti tizimutumikira ndi mtima wathu wonse chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Poganizira zimene munthuyo amakhulupirira, kodi mungamuthandize bwanji pogwiritsa ntchito mfundo ya palembali?

_____

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania